abale ache pamodzi ndi anthu ena zimene Mulungu wamuchitira.

-Mulungu akatimasula ife ku mphamvu ya satana ndi ziwanda zache, ndi kwabwino kwambiri kuti tidziŵawuza anthu ena zimene Mulungu akufunanso kuŵachitira iwowo.



# PHUNZIRO LA 56

1. Kodi fanizo ndi chiyani?
-Fanizo ndi nkhani imene imaphunzitsa zowona zenizeni za Malungu kwa anthu amene akufuna kumvetsetsa.

2. Kodi chifukwa chiyani Yesu anayamba kuŵaphunzitsa anthu m'mafanizo?
-Ngakhale kuti anthu ambiri ankamutsata Yesu, iwo sankamukhulupilira.

3. Kodi mu fanizoli, mbewu ndi chiyani?
-Mbewu ndi Mawu a Mulungu.

4. Kodi mu fanizoli, ofesa mbewu ndi ndani?
-Ofesa mbewu ndi munthu amene akulalikira Mawu a Mulungu.

5. Kodi anthu amene ali ngati njira ndi ati?
-Anthu amene ali ndi mitima yolimba.
-Mawu a Mulungu sangadutse m'mitima yawo.
-Kenako, Satana amabwera ndikudzatenga Mawu a Mulunguwo kuchokera kwa iwo.

6. Kodi anthu amene ali ngati nthaka ya pa tanthwe ndi ati?
-Pakamwa pawo ndi zochitika zawo amawoneka ngati amakhulupilira mwa Mulungu, koma m'mitima mwawo mulibe chikhulupiliro china chilichonse.

7. Kodi anthu amene ali ngati nthaka ya minga ndi ati?
-Anthu ameneŵa amalankhula kuti akukhulupilira mwa Mulungu, koma zofuna zawo zimakhala zofunika kwambiri kwa iwo kuposa Mulungu.

8. Kodi anthu amene ali ngati nthaka yabwino ndi ati?

-Anthu amenewa amati akamva Mawu a Mulungu, amafikira kuŵakhulupilira, ndikubereketsa zipatso zambiri.

-Yesu anapitiriza kuliphunzitsa khamu la anthu mpaka madzulo.

-Kenako Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anakwera mu ngalaŵa kuti awoloke Nyanja ya Galileya.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:35-37

35-Tsiku lomwelo, dzuŵa litaloŵa [Yesu] anaŵawuza ophunzira ache kuti, “Tiyeni tiwolokele ku tsidya linalo.”
36-Ndipo analisiya khamu la anthu, ndikumapita naye mu ngalaŵa muja, koma panali ngalaŵa zina zimene ankatsagana nazo.
37-Ndipo anayamba namondwe wankulu wa mphepo, ndipo mafunde ankafika mu ngalaŵayo, chomcho ngalaŵayo inayamba kudzadza.

-Kodi chinachitika ndi chiyani akuwoloka nyanja ija?
-Mphepo ya mkuntho inabwera.

-Mphepoyo imkawomba molimbika kwambiri, ndipo afunde anali okwera kwambiri mwakuti ngalaŵayo inatsala pang’ono kumila.

-Kodi Yesu anali kuti pa nthaŵi imeneyo?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:38a

38a-Yesu anali m’buyo mwa ngalaŵayo, atagona pa mtsamilo.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ankagona?



kuposa Mulungu.

-Yesu, Mulungu Mpulumutsi, anafika kudzaŵamasula kwa satana, koma iwo ankangoganiza za nkhumba zawo zokha.

-Leronso, anthu ambiri ali ngati anthu amenewo.

-Amangoganiza kwambiri za nkhumba zawo kuposa Yesu.

-Amangoganiza kwambiri za chuma chawo kuposa Yesu.

-Koma nkhumba kapena chuma zingakumasuleni inu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi satana?
-Ayi.

-Kodi kenako munthu amene anagwidwa ndi ziwanda uja anati chiyani kwa Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:18-20

18-Ndipo pamene Yesu anali kuloŵa mu ngalaŵa, munthu amene anagwidwa ndi ziwanda uja anamupenpha Yesu kuti atsagane naye kumene ankapita.
19-Ndipo Yesu sanamulole, koma anamuwuza kuti, “Pita kwanu kwa abale ako, ndipo ukaŵawuze zinthu zazikuru zimene Ambuye akuchitira, kutinso anakuchitira chifundo.”
20-Mchomcho munthu uja anapita nayamba kulalikira ku Dekapoli zinthu zazikuru zimene Yesu anamuchitira Iye, ndipo anthu onse anazizwa.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanamulole munthuyo kuti atsagane naye kumene ankapita?

-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti iye akaŵawuze

-Kodi anthu amene ankakhala ku dera limenelo atabwera anawona chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:15

15-Ndipo atafika kwa Yesu, anamuwona munthu amene anagwidwa ndi ziwanda uja atakhala pasi, atavala ndipo ali ndi nzeru zabwino, ndipo anthuwo anawopa.

-Kodi munthu amene anali ndi ziwanda uja anali kapolo wawobe?
-Ayi.

-Kodi amene anamupulumutsa munthu uja ku mphamvu ya ziwanda zija anali ndani?
-Yesu.

-Munthu uja sanalinso kapolo wa ziwanda.
-Munthu uja anamasulidwa ndi Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi anthu amene ankakhala ku dera limenelo anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:16-17

16-Anthu amene anaziwona zimene zinachitika aja, anaŵawuza anthu ena zimene zinachitika zija, za munthu wogwidwa ndi ziwanda ndi za nkhumba.
17-Ndipo anthu aja anamupenpha Iye kuti achoke m'malile awo.

-Kodi chifukwa chiyani anthuwo anamupempha Yesu kuti achoke ku deralo?
-Chifukwa chakuti anali opusa.
-Chifukwa chakuti ankaganiza kwambiri za nkhumba zawo



-Chifukwa chakuti anaŵaphunzitsa anthu kwa tsiku lonse latunthu , ndipo anatopa.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anatopa?
-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu weniweni, Iye analinso munthu weniweni.

-Kodi ophunzira a Yesu anachita chiyani atawona kuti ngalaŵa yawo yatsala pang'ono kumila?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:38b

38b- Ndipo ophunzira ache anamudzutsa Yesu aku-ti, "Mphunzitsi, kodi simusamala tikamila ife?"

-Ophunzira a Yesu anamudzutsa Yesu.

-Kodi ophunzira a Yesu anati chiyani kwa Yesu?
-"Kodi simusamala ife tikamila?"

-Kodi Yesu sankasamala?
-Yesu ankasamala kwambiri.

-Kodi Yesu anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:39

39- Yesu anadzuka ndipo anayiletsa mphepoyo, nati kwa nyanja, "Leka! Khala bata!"Ndipo mphepo inaleka, chomcho kunagwa bata lalikuru.

-Yesu anayilamula mphepo ya nkuntho kuti isisye.

-Kodi kenako chinachitika ndi chiyani?
-Mphepoyo inasiyilatu ndipo pa nyanjapo panali bata.

-Kodi zinatheka bwanji kuti Yesu ayilamule mphepo ya nkuntho kuti isiye?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.

-Kodi pachiyambi, analenga mphepo ndani?
-Yesu.

-Kodi pachiyambi, analenga nyanja ndani?
-Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani mphepo ndi nyanja zinamumvera Yesu?
-Chifukwa chakuti zinalengedwa ndi Yesu.

-Kodi Yesu analankhula chiyani mphepo itasiya ndipo nyanja itachita bata?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:40

40-Pomwepo anaŵafunsa ophunzira ache kuti, "Kodi chifukwa chiyani mukuchita mantha? Kodi mukadalibebe chikhulupiliro?"

-Yesu anaŵafunsa kuti kodi chifukwa chiyani analibe chikhulupiliro.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?

-Yesu ankaŵafunsa kuti kodi chifukwa chiyani iwowo sankakhulupilira kuti Iye anali Mulungu.

-Kodi kenako ophunzira  a Yesu anati chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 4:41

41- [Ophunzira ache] anachita mantha akuru, nafun-



Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:11-14

11-Ndipo panali guru lalikuru la nkhumba zimene zinkadya mphepete mwa phiri.
12-Ziwandazo zinamupempha Yesu kuti, "Kodi mungatitumize kwa nkhumbazo ndipo mutilore kuti tiloŵe mu izozo."
13-[Yesu] anazilora ziwandazo ndipo zinaturuka ndikuloŵa mu nkhumbazo. Kenako guru la nkhumbazo linatsikira ku nyanja mwa liwilo ndi kuloŵa m'nyanjamo ndipo zinamila, zinalipo ngati zikwi ziŵiri.
14-Anthu amene ankayang'anira nkhumbazo anathaŵa nakawuza anthu ku mudzi ndi ku minda ndipo anadza kudzawona zimene zinachitikazo.

-Chifukwa chakuti ziwanda zinamupempha Yesu, Iye anazilola kuti ziloŵe mwa nkhumba.

-Kodi pamene nkhumba zonse zinafa, ziwanda nazonso zinafa?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani ziwanda sizinafe?
-Chifukwa chakuti ziwanda ndi mizimu.
-Chifukwa chakuti ziwanda zilibe matupi ngati anthu kapena nyama.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanazitumize ziwanda ku Nyanja ya Moto Osatha?
-Chifukwa chakuti nthaŵi ya Mulungu yopelekera chilango kwa ziwanda inali isanakwane.

-Kumapeto kwache, Yesu adzamutumiza satana ndi ziwanda zache ku Nyanja ya Moto Osatha

-Kodi ziwanda zinkawopa chiyani?
-Zinkawopa kuti Yesu angazitumize ku Nyanja ya Moto Osatha.

-Kodi wamphamvu ndani kuposa satana ndi ziwanda zache?
-Mulungu.

-Mulungu adzamutumiza satana ndi ziwanda zache ku Nyanja ya Moto Osatha m'menre adzafunire.

-Kodi Yesu anati chiyani kwa ziwanda?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:8-10

8-Pakuti Yesu ananena kwa iye, Turuka iwe, mzimu wonyansa kwa munthuyu!"

9-Kenako Yesu anamufunsa iye kuti, "Kodi dzina lako ndani?" Ndipo anayankha kuti, "Ine dzina langa ndi Legio; chifukwa chakuti tilipo ambiri."

10-Ndipo anamupempha Iye kwambiri kuti asayitulutsile kunja kwa dzikolo.

-Kodi ziwanda zinadziŵa kuti sizingathe kumugonjetsa Yesu?
-Inde.

-Yesu ali ndi mphamvu zonse pa satana ndi ziwanda zache.

-Kumapeto kwache, Yesu adzamutumiza satana ndi ziwanda zache zonse ku Nyanja ya Moto Osatha.

-Ndi bwino kutumikira Mulungu kusiyana ndi ziwanda.

-Kodi kenako Yesu anachita chiyani?



sana wina ndi nzache kuti, "Kodi uyu ndi ndani nanga, wakuti ngakhale mphepo ndi nyanja zikumumvera Iye!"

-Ngakhale kuti ophunzira a Yesu amamuwona Iye akuchiza anthu odwala, sanamuwoneko Iye akuyilamula mphepo kuti isiye kulimbika.

-Ngakhale kuti ophunzira a Yesu amamuwona Iye akutulutsa ziwanda mwa anthu, sanamuwoneko Iye akuŵalamulila mafunde a pa nyanja kuti asiye.

-Palibe chimene angalephere kuchichita Yesu.
-Yesu ndi Mulungu.

-Pa tsiku lotsatira lachelo, Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anafika pa tsidya lina la nyanjayo.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:1-4

1-Ndipo anafika ku tsidya lina la nyanja, ku dziko la Agerasa.

2-Ndipo pamene anaturuka mu ngalaŵa, pomwepo anakumana ndi munthu wa ziwanda amene anachokera kumanda.

3-Munthuyu ankakhala kumanda, ndipo panalibe munthu amene anatha kumumanga iye ngakhale ndi unyolo.

4-Chifukwa chakuti wakhala akumangidwa kaŵiri-kaŵiri ndi mawunyolo koma wakhala akudula. Ndipo panalibe munthu amene anali ndi mphamvu yomugonjetsa iye.

-Kodi munthu ameneyu anakatha kudzipulumutsa yekha ku mphamvu ya ziwanda zimene zinkamulamulila iye?
-Ayi.

-Kodi anthu ena anakatha kumupulumutsa iye ku mphamvu ya ziwanda zimene zinkamulamulila iye?
-Ayi.

-Anthu ena ankayesa kumuthandiza iye pomumanga.

-Koma ziwanda zimene zinali mwa iye zinali zamphamvu kwambiri mwakuti zinkatha kudula mawunyolo amene ankamumanga nawowo.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:5

5-Ndipo masiku onse, usiku ndi usana, ankakhala m'manda ndi m'mapiri, ndi kumafuwula ndi kuzitematema ndi miyala.

-Kodi tingadziŵe bwanji kuti ziwanda zimaŵada anthu?
-Chifukwa chakuti zinkamukakamiza muthuyo kumakhala ku manda.

-Chifukwa chakuti zinkamukakamiza munthuyo kuti adzi-dziduladula yekha pa thupi lache.

-Ziwandazo zinamuchititsa munthuyo kukhala kapolo wawo.

-Ziwandazo zinkafuna kuti munthu ameneyu adziphe yek-ha.

-Chifukwa chakuti munthu ameneyu anali ndi ziwanda zambiri, izozo zinkamupweteka kwambiri.

-Inde, anthu tonse tinabadwa ngati munthu ameneyu, chifukwa chakuti tinabadwa ngati akapolo a ziwanda.

-Kodi mfumu ya ziwanda zonse ndi ndani?



-Satana.

-Satana ndi ziwanda zache zimaŵada anthu onse.
-Satana ndi ziwanda zache amangofuna kuwononga anthu basi.

-Ngakhale kuti satana ndi ziwanda zache amawoneka ngati akufuna kuŵathandiza anthu, amangochita zimenezi pongofuna kuŵawononga anthu.

-Mizimu imene imalamulila moyo wanu imawoneka ngati ikufuna kukuthandizani.
-Koma imachita zimenezi pongofuna kukuwonongani.

-Satana ndi ziwanda zache ali ndi cholinga chimodzi cho-kha m'moyo wanu.
-Ichi ndi kuwononga anthu ambiri m'mene angathere.

-Satana ndi ziwanda zache sakufuna kuti inu mumudziŵe Mulungu kuti mupulumutsidwe ku mphamvu yawo.
-Kodi chinachitika ndi chiyani munthu ameneyu ata-muwona Yesu

Tiyeni tiŵerenge Maliko 5:6-7

6-Ndipo atamuwona Yesu potalikirapo, anathaman-ga namugwadira Iye.
7-Ndipo anafuwula molimbika kwambiri nati, "Ukufuna chiyani ndi ine, Yesu, Mwana wa Mulungu wapamwambamwamba? Lumbirani kwa Mulungu kuti simundizunza ine!"

-Kodi ziwanda zinkadziŵa kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi?
-Inde.